

THE TRIPLE S SYSTEM

Njira yakasungidwe ka mbatata yomwe tifotokoze apayi, imathandiza kuti alimi akhale ndi mbeu yochuluka panthawi yoyenera. Nthawi zambiri, alimi amapeza mbeu ya mbatata kuchokera ku mphukira.

Mitsisi kapena mbatata ing'onoing'ono yomwe singagulitsidwe pa msika imatsala m'munda pokolola. Ndipo:

1. Mitsisiyi imamera mvula ikagwa ngati imatsala m'munda muja pokumba.
2. Koma mbeu yochokera ku mitsisi ndiyosadalilika chifukwa imamera patalipatali komanso siyotetezedwa ku ziweto ndi anthu akuba.

Akatswiri aza ulimi pamodzi ndi alimi apeza njira yochuluktsira mbeu kuchokera ku mitsisi ya mbatata ing'onoing'ono poyisunga mu m'chenga. Mbatatayi imadzaphuka ndikupereka mbeu yambiri panthawi yobzala m'munda.




University of Greenwich, Central Avenue,
Chatham Maritime, Kent, ME4 4TB, UK

International Potato Center (CIP) – UGANDA,
P.O. Box 22274, Kampala, Uganda

CIP Sub Saharan Regional Office, c/o ILRI,
P.O. Box 25171, Nairobi 00603, Kenya

CIP Malawi, PO Box 31600 Lilongwe 3
Contact address: p.abidin@cgiar.org



MBEU ya Mbatata

THE TRIPLES
SYSTEM

Storage
Sand
Sprouting



Kukolola mbatata

1

Kumapeto kwa mvula, alimi amasankha mbatata ing'onoing'ono pokolola, yopanda matenda komanso nankafumbwe wa Mbatata



Kuwola mchenga

2

Pakapita milung 6 kapena 8 mbeu imakhala itaphukira.




3



Sungani chosungira mbatata yanu pa malo ozizira bwino, komanso posafikira ana kapena ziweto. Mphukira zimakhala zofupikirapo koma ngati mvula ili patali titha kuthena mphukirazo kuti mbatata iphukirenso moyembekezera mvula.

4



Pakapita milungu 6 kapena 8 **tikhoza kubyala Mbatata yophukira ija ku munda kwathu**
Kwirirani Mbatata yonse ndi mphukira zomwe. Byalani pa mulingo wa 50cm pa phando, mizere yotalikirana 50cm, ikani kachidikha kothandiza pothilira. Dothi likhale la chonde. Tetezani mbeu kuziweto. Thiliran pakapita masiku awiri kapena atatu, molingana ndi m'mene mukulionera dothi.

5



Mvula ikayamba kugwa, mbatata imaphukira kwambiri, kotero mutha kumadulako mbeu ndikuonjezera malo olima.

mbatatayi 40 ikhoza kupereka mbeu yochuluka 1500



Yalani mchenga mulingo wokwanira 5 cm

